**Kodi ndi chifukwa chiyani kukhulupirika kuli kofunikira kwambiri ngati ndasankha kugwiritsa ntchito ling'i mukafukufuku wa HOPE?** Kukhulupirika kwambiri kunali kofunikira mu kafukufuku wa ASPIRE pofuna kuona ngati ling'i yokhala ndi mankhwala a dapivirine inali yoteteza amai ku HIV. Mu kafukufuku wa HOPE, kukhulupirika kwambiri kumeneku ndikofunika chifukwa kukukhudza mulingo wakuziteteza kwanu ku HIV.

**Ngati nditamagwiritsa ntchito ling'i nthawi zonse, ndidzatetezedwa kufika pa mulingo uti?** Tikudziwa kuti chitetezo ku HIV chimachuluka pamene ling'i ikugwiritsidwa ntchito nthawi zonse, komanso kuti ling'i siyimapereka chitetezo ngati siikugwiritsidwa ntchito. Nkofunika kudziwa kuti ngati mumabvalira ling'i nthawi yambiri, koma nkupezeka kuti siili m'malo mwake nthawi yomwe muli pa chiopsyezo chotenga HIV (mwachitsanzo ngati mwaichotsa panthawi yomwe mukugonana), simungatetezedwe. Pamene wofufuza analengeza zotsatira za ASPIRE, anali asanawunike mmene kubvalira ling'i kumakhudzana ndi mmene ling'i ikugwilira ntchito yoteteza. Tsopano akhala ndi nthawi yoyang'ana funsoli. Uthenga watsopano omwe kafukufuku wa ASPIRE wapeza ndi oti ngati ling'i ikugwiritsidwa ntchito nthawi zambiri, anthu 75 pa anthu 100 aliwonse kapena kupyolerapo atha kutetezeka ndipo ngati ling'i ikugwiritsidwa ntchito nthawi zonse, anthu 90 pa anthu 100 aliwonse kapena kupyolerapo atha kutetezeka. Zotsatira za kafukufuku wa HOPE zidzathandiza ofufuza kumvetsetsa kwambiri za mulingo wachitetezo omwe ling'i itha kupereka ngati itagwiritsidwa ntchito nthawi zonse.

**Pophera nkota, ndi chifukwa chiyani kukhulupirika kuli kofunikira mukafukufuku wa HOPE?** Kugwiritsa ntchito ling'i nthawi zonse pakati pa amai omwe asankha ling'i kudzatithandiza kumvetsetsa kwambiri zokhudza kugwira ntchito kwake ngati ling'i ikugwiritsidwa ntchito nthawi zonse. Uthenga umenewu ndi ofunika kwambiri kuudziwa maka pokonzekera chiyambi chobweretsa ling'i imeneyi kwa anthu onse.

**Chidzachitike ndi chiyani ngati ndizakhale ndi zopinga pakugwiritsa ntchito ling'i ya mukafukufuku wa HOPE?** Ogwira ntchito kukafukufuku wa HOPE akufuna kuti inu mupange dongosolo lomwe mungakwanitse kulitsatira la mmene mungazitetezere ku HIV. Ngati musankhe



kugwiritsa ntchito ling'i kenaka nkupezeka kuti zikukuvutani kugwiritsa ntchito kwake, aphungu amukafukufuku adzakuthandizani za mmene mungagonjetsere zovuta zimenezo. Ngakhale mutasankha kusagwiritsa ntchito ling'i, kapena mwasitha maganizo pazakugwiritsa ntchito ling'i, aphungu akukafukufuku adzakuthandizani pa dongosolo lirilonse lomwe mungasankhe lokhudza kudziteteza ku HIV.

**Kodi zidzakhala bwanji ngati mzanga kapena wina wa m'banja langa akufuna kugwiritsa ntchito ling'i?** Pakadali pano, ling'i ikuperekedwa kwa amai okhawo omwe alowa mukafukufuku wa HOPE. Nkofunikira kwambiri kuti musagawane ling'i kapena kumpatsa wina. Amai omwe sali mukafukufuku sangathe kupeza mwayi oyezedwa pafupipafupi za HIV komanso mimba, kapena kulandira thandizo la chipatala monga zikuyenera kukhalira. Ngati angagwiritse ntchito ling'i kenaka ndikupezeka ndi mavuto, atha osapeza thandizo lomwe angalifune. Ling'i itha kukutetezani pokhapokha mutamaigwiritsa ntchito nthawi zonse, izi zikutanthauza kuti simukuyenera kupatsa ena.

**Kodi amene analowa kafukufuku wa ASPIRE koma samakhulupirika adzaloredwanso kulowa mukafukufuku wa HOPE?** Onse omwe analowa kafukufuku wa ASPIRE adzapatsidwa mwai olowa kafukufuku wa HOPE. Tikuwayamika kwambiri onse omwe analowa kafukufuku wa ASPIRE amene anathadiza kuti tionetse kuti ling'i ndi yosaopsya kuigwiritsa ntchito komanso yothandiza kuchepetsa chiopsyezo chotenga HIV. Tikudziwa kuti pali ena omwe analowa kafukufukuyu kuti panali zovuta zina zomwe zinawapangitsa kuvutika kugwiritsa ntchito ling'i kapena anasankhanso kusaigwiritsa ntchito. Mukafukufuku wa HOPE, tikufuna kuti onse omwe analowa mukafukufuku wa ASPIRE "ayambenso mwatsopano" ndipo akhale ndi mwai ochepetsa chiopsyezo chotengera HIV mmene angathere. Pa chifukwa ichi, tikufuna tipereke ling'i imeneyi komanso zina zomwe angathe kupindula nazo kwa omwe analowa kafukufuku wa ASPIRE.

**Kodi ling'i imeneyi idzagwira ntchito mofanana kwa amai a misinkhu yonse?** Mu ASPIRE, amayi amene zaka zawo zinali 21 ndi kucheperako omwe

anali mugulu logwiritsa ntchito ling'i ya Dapivirine anatenga HIV mofanana ndi amayi omwe anapatsidwa ling'i yongoyerekezera. Komabe, tikudziwa kuti chomwe chinapangitsa kuti ling'i ya Dapivirine isagwile ntchito pakati pa amayi achichepere mu ASPIRE kunali kusagwiritsa ntchito nthawi zonse. Ofufuza ali mkati mopanga akafukufuku ena kuti apeze ngati pali zinthu zina zomwe zitha kukhudza kagwiridwe ntchito ka ling'i kwa amai achichepere. Nkofunika kudziwa kuti amai onse omwe anatenga nawo mbali mukafukufuku wa ASPIRE adzakhala ali ndi zaka zoposa 21 pamene idzifike nthawi yolowa mukafukufuku wa HOPE. Ziri kwa ife ngati ogwira ntchito kukafukufuku, otenga nawo mbali mukafukufuku, komanso anthu mmaderamu, kulimbikitsa amai achichepere mu njira yabwino kuti athe kupeza komanso kugwiritsa ntchito mokhulupirika njira zodalirika zopewera kutenga HIV zimene zili zokomera moyo wawo.

Ngati muli ndi mafunso kapena mukufuna uthenga wochulukirapo, chonde pitani ku kiliniki ya kafukufuku:

Version 1.0, CHICHEWA, 16NOV2016

HOPE

HIV Open-label Prevention Extension

*Out of ASPIRE, there is HOPE*

# KUKHULUPIRIKA PA KUGWIRITSA NTCHITO LING'I KOMANSO KUDZITETEZA KU HIV MUKAFUKUFUKU WA HOPE

